



**KODI NDINE YANI KUTI**

**MFUMU**

**ADAYENERA KUFA**

**M'MALO MWANGA?**

Lokonzedwa ndi  
Watson Goodman

Laulere—Losayenera  
Kugulitsidwa

## **KODI NDINE YANI?**

**Mlengi wathu amadziwa amene ife tiri, zonse zafotokozedwa bwino m'MAU AKE a muyaya m'mene tingapeze “m'mene tidapangidwira”, “nanga tidakhala chiyani”, “kumene titsogoleredwa”, ndi “chimene tingakhale” pakubvomereza chiombolo cha Mulungu.**

**Ena sakudziwa za chiombolo cha Mulungu. Ena amachidziwa pang'ono ndipo asowa kufunsa mosamalitsa kuti achidziwe bwino. Ena amalimbana ndi chiombolo cha Mulungu nachikana kotheratu, pamene ena akuchikhumbatira ndi mtima wonse ndipo mu kuomboledwa akupeza kuti mwa Yesu Khristu akhala munthu wa pamwamba mu chimaliziro chake chamuyaya.**

**Moyo wanga wamuyaya ndi woyenera kwenikweni pa zimene ine ndigamulolere Mlengi wanga kuupanga mwa Iye yekha! Izi ziri monga kumkana Iye ndipo zotsatira zake zikhala zopanda pake mu umuyaya wosatha, kapena chibvomerezo ndi kumvera mokhulupirika, kumulola Iye kutipangitsa ife kugawana naye Mpando wake wachifumu wamuyaya m'mwamba.**

**—Watson Goodman (1920-2002)**

# CHOLINGA CHACHIKURU CHA MULUNGU

## POLENGA MUNTHU

1

Iye Adzakhala Ndi Mkwatibwi  
Wamuyaya

**Yesaya 62.5b**

. . . ndi monga mkwati ako-  
ndwera ndi mkwatibwi, momwe-  
mo Mulungu wako adzakondwera  
nawe.

**Mateyu 25.1, 6**

Pomwepo Ufumu wa Ku-  
mwamba udzafanizidwa ndi ana-  
mwali khumi, amene adatenga  
nyali zawo, naturuka kukakoma-  
na ndi mkwati. . . Koma paka-  
ti pa usiku panali kupfuula, O-  
nani, mkwati! turukani kukako-  
mana naye.

Khristu — Mkwati

**2 Akorinto 11.2**

Pakuti ndichita nsanje pa inu  
ndi nsanje ya Mulungu; pakuti  
ndidakupalitsani ubwenzi mwa-  
muna mmodzi, kuti ndikalangi-  
ze inu ngati namwali woyera  
mtima kwa Khristu.

**Mateyu 9.15**

Ndipo Yesu adati kwa iwo,  
Nanga anyamata a nyumba ya  
ukwati angathe kulira kodi nth-  
wi imene mkwati akhala nawo?  
koma adzafika masiku, pamene  
mkwati adzachotsedwa kwa iwo,  
ndipo pomwepo adzasala kudya.

## **2 ICHI NDI CHIFUKWA CHAKE MULUNGU ADAPANGA MUNTHU MU CHIFANIZIRO CHAKE**

Palibe Munthu Wotsika Kuposera Apa Amene Akadayenera Kulantira Ulemu Wakukhala Mkwatibwi

Mulungu ndipo adalenga munthu m'chifanizo chake m'chifanizo cha Mulungu adamlenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mka-zi. — Genesis 1.27

Monga adatisankha ife mwa Iye, lisadakhazikike dziko lapansi, tikhale ife oyera mtima, ndi opanda chirema pamaso pake m'chikondi. — Aefeso 1.4

Woyenera Kudya Nawo Phwando La Mulungu

. . . kuti mwa izi mukakhale oyanjana nawo umulungu wace . . . — 2 Petro 1.4b . . . ndinonso wolawana nawo ulemerero udzabvumbulutsikawo. — 1 Petro 5.1b . . . ndi olandira nafe pamodzi palonjezano mwa Khristu Yesu, mwa Uthenga Wabwino. — Aefeso 3.6b . . . amene adatiyeneretsa ife kulandirana nawo hcolowa hca oyera mtima m'kuunika. — Akolose 1.12b . . . Pakuti takhala ife olandirana ndi Khristu . . . — Ahebri 3.14a . . . nakhala olandirana naye Mzimu Woyera. — Ahebri 6.4b

## INE NDINE MPHUKIRA YA MULUNGU

3

Genesis 9.6b

... chifukwa m'chifanizo cha Mulungu Iye adampanga munthu.

Mahcitidwe A Atumwi

17.24a, 25b, 26a, 27-29

Mulungu amene adalenga dziko lapansi ndi zonse ziri momwemo. . . popeza Iye mwini apatsa zonse moyo ndi mpweya ndi zinthu zonse; ndipo ndi mmodzi adalenga mitundu yonse ya anthu. . . kuti afunefune Mulungu, kapena akamfufuze ndi kumpeza, ngakhale sakhala patari ndi yense wa ife; pakuti mwa Iye tikhala ndi moyo ndi kuyendayenda, ndi kupeza mkhalidwe wathu; monga enanso a akuyimba anu

ati, Pakuti ifenso tiri mbadwa zake. Popeza tsono tiri mbadwa za Mulungu, sitiyanera kulingalira kuti umulungu uli wofanafana ndi golidi, kapena siliva, kapena mwala, wolocha ndi luso ndi zolingalira za anthu.

Adamu, Wopangidwa M'chifaniziro Cha Mulungu, Adaonetsera Ulemelero Monga Ulemelero Wa Mulungu

1 Mafuma 8.11

Ndipo ansembe sadakhoza kumirira kutumikira chifukwa cha mtambowo, popeza ulemmerero wa Yehova unadzaza nyumba ya Yehova.

## 4 KUCHOKERA KU CHIYERO KUPITA KU UCHIMO NDI MDIMA

Pakuti onse adachimwa, nape-  
reŵera pa ulemerero wa Mulu-  
ngu. — Aroma 3.23

1 Petro 1.16

Popeza kwalembedwa, Muzi-  
khala oyera mtima, pakuti Ine  
ndine woyera mtima.

Aroma 5.19

Pakuti monga ndi kusamvera  
kwa munthu mmodzi ambiri  
adayesedwa ochimwa, chomwe-  
cho ndi kumvera kwa mmodzi  
ambiri adzayesedwa olungama.

Yeremiya 17.9

Mtima ndiwo wonyenga kopo-  
sa, ndi wosachiritsika, ndani  
angathe kuudziŵa?

Ndipo adaona Yehova kuti kui-  
pa kwa anthu kunali kwakukuru  
pa dziko lapansi, ndiponso kuti  
ndingaliro zonse za maganizo a  
mitima yawo zinali zoipabe zo-  
khazokha. — Genesis 6.5

. . . Ndinena kwa inu, sindidzi-  
ŵa kumene muchokera inu; cho-  
kani pa Ine, nonse akuchita cho-  
salungama. — Luka 13.27b

Yohane 3.19

Koma chiŵeruziro ndi ichi,  
kuti kuunika kunadza ku dziko la-  
pansi, ndipo anthu adakonda  
mdima koposa kuunika; pakuti  
ntchito zawo zinali zoipa.

## **TSOPANO PALI UBALE WANJI NDI MULUNGU? 5**

Thupi Lanyama Lakufa Liri  
Lodetsedwa (Lonyansa)

**Yesaya 64.6a**

**Pakuti ife tonse takhala ngati  
wina amene ali wosakonzeka. . .**

**Imfa Ya Muyaya Iri Pa Ine**

**Chifukwa chake, monga uchi-  
mo udaloŵa m'dziko lapansi mwa  
munthu mmodzi, ndi imfa mwa  
uchimo; chotero imfa idafikira a-  
nthu onse, chifukwa kuti onse  
adachimwa. — Aroma 5.12**

**Ine Ndatsutsidwa**

**Aroma 5.18a**

**Chifukwa chake, monga mwa  
kulakwa kumodzi kutsutsa kuda-  
fikira anthu onse. . .**

Tchimo Lindipangitsabe Ine  
Kukhala Kapolo

**Aroma 7.23**

**Koma ndiona lamulo lina m'zi-  
ŵalo zanga, lirikulimbana ndi la-  
mulo la mtima wanga, ndi kundi-  
gonjetsa kapolo wa lamulo la  
m'ziŵalo zanga.**

**Tchimo Lisiyanitsa Ndi Mulungu**

**Yesaya 59.2a**

**Koma zoipa zanu zakulekani-  
tsani inu ndi Mulungu wanu. . .**

**Ine Ndiri Ndi Udindo**

**Kwa Mulungu**

**Chotero munthu ali yense wa  
ife adzadziŵerenga mlandu wa-  
ke kwa Mulungu. —Aroma 14.12**

M'thupi Lanyama Lakufa, Ndiri  
Ngati Dothi Udzu, Nthunzi

**Koma tsopano, Yehova, Inu ndinu Atate wathu; ife tiri dongo, ndipo Inu ndinu Muumbi wathu; ndipo ife tonse tiri ntchito ya dzanja lanu. — Yesaya 64.8**

Popeza, Anthu onse akunga udzu, Ndi ulemmerero wawo wonse ngati duwa la udzu. Udzuwo ungofofa, ndi duwa lake lingo-gwa. — 1 Petro 1.24

Inu amene simudziwa chime-ne chidzagwa maŵa. Moyo wanu uli wotani? Pakuti muli utsi, wakuonekera kanthaŵi, ndi pamene-po ukanganuka. — Yakobo 4.14

Ndingathe Kukhala Wosafa Ndi Moyo Wosatha Mwa Khristu

**Ndipo yense wakukhala ndi moyo, nakhulupirira Ine, sadzamalira nthawi yonse. Kodi ukhulupirira ichi? — Yohane 11.26**

**I Yohane 5.10, 11**

Iye amene amkhulupirira Mwana wa Mulungu ali nawo umboni mwa iye; iye wosakhulupirira Mulungu adamuyesa Iye wonama: chifukwa sadakhulupirira umboni wa Mulungu adauchita wa Mwana wake. Ndipo uwu ndi umboniwo, kuti Mulungu adati-patsa ife moyo wosatha, ndipo moyo umene uli mwa Mwana wake.



## KODI MFUMU YA ULEMELERO NDIYE YANI? 7

Masalmo 24.7-10

Weramutsani mitu yanu, zipata inu; Ndipo kwezekani inu, zitseko zosatha: Kuti Mfumu ya ulemerero iloŵe. Mfumu imene ya ulemerero ndani? Yehova wamphamvu ndi wolimba, Yehova wolimba kunkhondo. Weramutsani mitu yanu, zipata inu; Inde weramutsani, zitseko zosatha inu, Kuti Mfumu ya ulemerero iloŵe. Mfumu imene ya ulemerero ndani? Yehova wa makamu makamu, Ndiye Mfumu ya ulemerero.

1 Timoteo 6.14b, 15b, 16

. . . Kufikira maonekedwe a Ambuye wathu Yesu Khristu . . . amene ali Mwini Mphamvu woda-

la ndi wayekha, ndiye Mfumu ya mafumu ndi Mbuye wa ambuye; amene Iye yekha ali nawo moyo wosatha, wakukhala m'kuunika kosakhozeka kufikako; amene munthu sanamuona, kapena sakhoza kumuona; kwa Iye kukhale ulemu ndi mphamvu yosatha. Amen.

Mfumu Ameneyi Adzakhala  
Mfumu Pa Dziko Lonse  
Lapansi

Zekariya 14.9

Ndipo Yehova adzakhala mfumu ya dziko lonse; tsiku lomwelo Yehova adzakhala Iye yekha, ndi dzina lake ilo lokha.

## 8 YESU KHRISTU ALENGEZA ZA UFUMU WAKE

Yohane 18.36, 37

Yesu adayankha, Ufumu wanga suli wa dziko lino lapansi; ufumu wanga ukadakhala wa dziko lino lapansi, anyamata anga akadalimbika nkondo, kuti ndisaperekedwe kwa Ayuda; koma tsopano ufumu wanga suli wochoke-ra konkuno. Pamenepo Pilato anati kwa Iye, Nanga kodi ndiwe Mfumu? Yesu adayankha, Muna kuti ndine Mfumu. Ndinabawira ichi Ine, ndipo ndinadzera ichi kudza ku dziko lapansi, kuti ndikachite umboni ndi choonadi.

Marko 14.61, 62

Mkulu wa anembe anamfun-sanso... Kodi Iwe ndiwe Khri-

stu, Mwana wake wa Wolemekezeka? Ndipo Yesu anati, Ndine amene; ndipo mudzaona Mwana wa munthu alikukhala ku dzanja lamanja la mphamvu, ndi kudza ndi mitambo ya kumwamba.

Koma pamene Mwana wa munthu adzadza mu ulemmerero wake, ndi angelo onse pamodzi naye, pomwepo Iye adzakhala pa chimpando cha kuwala kwake... Pomwepo Mfumuyo idzanena kwa iwo a ku dzanja lake lamanja, Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, loŵani mu Ufumu wokonzedwera kwa inu pa chikhazikiro chake cha dziko lapansi. — Mateyu 25.31, 34

## **MKHALIDWE WAKE WA UFUMU WA YESU KHRISTU 9**

### **Ahebri 1.8**

Koma ponena za Mwana, ati, Mpando wachifumu wanu, Mulungu, ufikira nthawi za nthawi; Ndipo ndodo yachifumu yoongoka ndiyo ndodo ya ufumu wanu.

### **Chibvumbulutso 11.15b**

... Ufumu wa dziko lapansi walyamba kukhala wa Ambuye wathu, ndi wa Khristu wake: ndipo adzacita ufumu kufikira nthawi za nthawi.

### **Aefeso 1.18, 19**

Ndiko kunena kuti maso a mitima yanu awalitsike, kuti mukadziwe inu chiyembekezo cha kuitana kwake nchiyani; nchiyaninso cuma cha ulemerero wa

choloŵa chake mwa oyera mtima, ndi chiyani ukuru woposa wa mphamvu yake ya kwa ife okhulupira.

Ngati simutembenuka, nimukhala monga tianato, simudzalowa oknse mu Ufumu wa Kumwamba. Chifukwa chake yense amenyadzichepetsa yekha monga kamwana aka, yemweyo ali wopambana mu Ufumu wa Kumwamba. — Mateyu 18.3, 4

### **Danieli 4.37**

Tsono ine Nebukadinezara ndiyamika, ndi kukuza, ndi kulemekeza Mfumu ya Kumwamba, pakuti ntchito zake zonse nzoonna, ndi njira zake chiweruzo...

## 10 MAKHALIDWE AKE A MFUMU YA ULEMELERO

### Yohane 17.2

Monga mwampatsa Iye ulamuliro pa thupi liri lonse, kuti onse amene mwampatsa Iye, awapatse iwo moyo wosatha.

### 1 Petro 3.22

Amene akhala pa dzanja lamanja la Mulungu, ataloŵa m'Mwamba; pali angelo, ndi maulamuliro, ndi zimphamvu, zomgonjera.

### Aefeso 1.20-23

Imene adachititsa mwa Khristu, m'mene anamuukitsa kwa akufa, namkhazikitsa pa dzanja lake lamanja m'zakumwamba, pamwamba pa ukulu wonse, ndi ulamuliro, ndi mphamvu, ndi ufumu, ndi dzina liri lonse lotche-

dwa, si m'nyengo yino ya pansipano yokha, komanso mwa iyo ikudza; ndipo adakonza zonse pansipano pa mapazi ake, namwampatsa Iye akhale mutu pamtu pa zonse, kwa Eklesia amene ali thupi lake, mdzazidwe wa Iye amene adzaza zonse m'Zonse.

### Yohane 2.24a, 25b

Koma Yesu sanakhulupirira iwo kuti akhale nawo... pakuti anadziŵa Iye yekha chimene chinali mwa munthu.

### Yohane 17.23b

...kuti dziko lapansi lizindikire kuti Inu munandituma Ine, nimudawakonda iwo, monga momwe mudakonda Ine.

## **CHUMA, MPHAMVU, NDI NZERU ZOSATHA 11**

### **Chibvumbulutso 5.12b**

. . . Ayenera Mwanawankhosa, wophedwayo, kulandira chilimbiko, ndi chuma, ndi nzeru, ndi mphamvu, ndi ulemu, ndi ulemero, ndi chiyamiko.

### **Mateyu 28.18**

Ndipo Yesu anadza nalankhula nawo, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi.

Koma kwa ife kuli Mulungu mmodzi, Atate amene zinthu zonse zichokera kwa Iye, ndi ife kufikira kwa Iye; ndi Ambuye mmodzi Yesu Khristu, amene zinthu zonse ziri mwa Iye, ndi ife mwa Iye. — 1 Akorinto 8.6

Koma kwa iwo oitanidwa, ndiwo Ayuda ndi Ahelene, Khristu mphamvu ya Mulungu, ndi nzeru ya Mulungu. — 1 Akorinto 1.24

### **Chibvumbulutso 11:17**

Nati, Tikuyamikani, Ambuye Mulungu, Wamphamvuyonse, amene muli, nimunali; popeza mwadzitengera mphamvu yanu yaikuru, ndipo mwachita ufumu.

### **Akolose 2.2, 3**

Kuti itonthozeke mitima yawo, nalumikizike pamodzi iwo m'chikondi . . . kuti akazindikire iwo chinsinsi cha Mulungu, ndiye Khristu, amene zolemera zonse za nzeru ndi chidziwitso zibisika mwa Iye.

## 12 CHITSOGOLO CHA MFUMU YA ULEMELERO

Masalmo 72.8, 11

Ndipo adzachita ufumu kuchokera kunyanja kufikira kunyanja, Ndi kuchokera ku Mtsinje kufikira malekezero a dziko lapansi . . . Inde mafumu onse adzangwadira iye: Amitundu onse adzamtumikira.

Masalmo 2.2-4, 6-8

Adzikhazikitsa mafumu a dziko lapansi, Nachita upo akulu pamodzi, Kutsutsana naye Yehova, ndi Wodzozedwa wake, ndi kuti, Tidule zomangira zawo, Titaye nsinga zawo. Wokhala m'mwambayo adzaseka; Ambuye adzawanyoza . . . Koma Ine ndadzoza

mfumu yanga Pa Ziyoni, phiri langa loyera. Ndidzauza za chitsimikizo: Yehova ananena ndi Ine, Iwe ndiwe Mwana wanga; Ine lero ndakubala. Undifunse, ndipo ndidzakupatsa amitundu akhale choloŵa chako, Ndi malekezero a dziko lapansi akhale ako.

Yeremiya 10.7, 10a

Wosaopa Inu ndani, Mfumu ya amitundu? Pakuti kukuopani ndi kwanu; pakuti mwa anzeru onse a amitundu, ndi m'maufumu awo onse, mulibe akunga Inu. . . Koma Yehova ndiye Mulungu wonna; ndiye Mulungu wamoyo, mfumu yamuyaya. . .

**Yesaya 42.8**

Ine ndine Yehova; dzina langa ndi lomweli; ndipo ulemerero wanga Ine sindidzapereka kwa wina, ngakhale kunditamanda kwa mafano osemedwa.

**Masalmo 95.3**

Pakuti Yehova ndiye Mulungu wamkuru; Ndi mfumu yaikuru yoposa milungu yonse.

**Mateyu 24.30b**

... ndipo mitundu yonse ya pa dziko lapansi idzadziguguda pachifuwa, nidzapenya Mwana wa munthu alinkudza pa mitambo ya kumwamba, ndi mphamvu ndi ulemerero waukuru.

**Chibvumbulutso 4.11**

Muyenera inu, Ambuye wathu, ndi Mulungu wathu, kulandira ulemerero ndi ulemu ndi mphamvu; chifukwa mudalenga zonse, ndipo mwa chifuniro chanu zinalakhalana, nizinalengedwa.

Ndipo kwa Mfumu yosatha, yosabvunda, yosaoneka, Mulungu wa yekha, ukhale ulemu ndi ulemerero, kufikira nthawi za nthawi. Amen. — 1 Timoteo 1.17

Akugawana Ulemelero Wake  
Ndi Mkwatibwi

**Yohane 17.22**

Ndipo ulemerero umene mwandipatsa Ine ndapatsa iwo...

## 14 MFUMU MLENGI ALI KULAMULIRA

**Yesaya 9.7a**

Za kuenjezera ulamuliro wake, ndi za mtendere sizidzatha pa mpando wachifumu...

**Yesaya 45.9a, 10-13a**

Tsoka kwa iye amene akangana ndi Mlengi wake!... Tsoka kwa iye amene ati kwa atate wake, Kodi iwe ubalanji? pena kwa mkazi, Ulikusauka ninji iwe? Atero Yehova Woyera wa Israyeli ndi Mlengi wake, Ndifunse Ine za zinthu zimene zirinkudza; za ana anga amuna, ndi za ntchito ya manja anga, ndilamulireni Ine. Ine ndalenga dziko lapansi, ndalengamo munthu; Ine, ngakhale manja anga, ndafunyulula

kumwamba, ndi zonse za m'menemo, ndinazilamulira ndine. Ine ndautsa Koresi m'chilungamo, ndipo ndidzalungamitsa njira zake zonse...

Ndipo adampatsa ulamuliro, ndi ulemerero, ndi ufumu, kufi anthu onse, ndi mitundu yonse ya anthu, ndi a manenedwe onse, amtumikire; ulamuliro wake ndi ulamuliro wosatha wosapitirira, ndi ufumu wake sudzawonongeka. — Danieli 7.14

Lolerani Ulamuliro Wake

Inde mafumu onse adzangwadirira iye: Amitundu onse adzamtumikira. — Masalmo 72.11



## MFUMU YA ULEMELERO ADAFA CHIFUKWA 15 CHA INE!

Adaloseru Kale Za Malo Ndi  
M'mene Akadafera Ndi Kuuki-  
tsidwa Kuchokera Kwa Akufa  
Mateyu 20.18, 19

Onani, tikwera ku Yerusalemu;  
ndipo Mwana wa munthu adza-  
perekedwa kwa ansembe akuru  
ndi alembi, ndipo iwo adzamuwe-  
ruza kuti ayenera imfa, nadza-  
mpereka kwa anthu akunja kuti  
amnyoze ndi kumkwapula, ndi ku-  
mpachika; ndipo Iye adzaukitsu-  
dwa tsiku lachitatu.

Tchimo Ndi Loopsya Kwambiri  
M'maso Mwa Mulungu Potosoŵa  
Makonzedwe Oterewa

Pakuti Khristunso adamva zo-

ŵaŵa kamodzi, chifukwa cha ma-  
chimo, wolungama m'malo mwa  
osalungama, kuti akatifikitse kwa  
Mulungu; wophedwatu m'thupi,  
koma wopatsidwa moyo mumzi-  
mu. — 1 Petro 3.18

. . . ndi Ambuye wathu Yesu  
Khristu, amene anadzipereka ye-  
kha chifukwa cha machimo athu,  
kuti akatilanditse ife m'nyengo ya  
pansi pano yino yoipa, monga  
mwa chifuniro cha Mulungu ndi  
Atate wathu.— Agalatiya 1.3b, 4

1 Yohane 3.16a

Umo tizindikira chikondi, po-  
peza Iyeyu adapereka moyo wake  
chifukwa cha ife . . .

## 16 MWAZI WAMTENGO WAKE — MPULUMUTSI WOPAMBANA

**Aefeso 2.13**

Koma tsopano mwa Yesu Khristu inu amene munali kutali kale, anakusendezani mukhale pafupi m'mwazi wa Khristu.

**Ahebri 10.19, 20a**

Ndipo pokhala nacho, abale, chilimbikitso chakuloŵa m'malo opatulika, ndi mwazi wa Yesu, pa njira yatsopano ndi yamoyo. . .

. . . ndi mwazi wa chipangano chosatha. . . — Ahebri 13.20b

**Akolose 1.20b**

. . . atachita mtendere mwa mwazi wa mtanda wake. . .

**Chibvumbulutso 1.5b**

Kwa Iye amene atikonda ife, natimasula ku machimo athu ndi mwazi wake.

**1 Petro 2.6b, 7a**

. . . Taona, ndiika m'Ziyoni mwala wotsiriza wa pangondya, wosankhika, wa mtengo wake; Ndipo wokhulupirira Iye sadza-nyazitsidwa. Kwa inu tsono aku-khulupira, ali wa mtengo wake.

Mkwati Afunafuna Mkwatibwi  
Wake

Pakuti Mwana wa munthu ana-dza kufunafuna ndi kupulumutsa chotayikacho. — Luka 19.10

## **KHRISTU ANAGONJETSA IMFA YACHIWIRI NDI 17 GEHENA; KUNDIPULUMUTSA INE KUCHOKERA KU IZO**

Ndidayenera Ine Kulandira  
Imfa Ya Muyaya

...moyo wochimwawo ndiwo  
udzafa. — Ezekeili 18.4b

Chifukwa chake, monga uchi-  
mo udaloŵa m'dziko lapansi mwa  
munthu mmodzi, ndi imfa mwa  
uchimo; chotero imfa idafikira  
anthu onse, chifukwa kuti onse  
adachimwa. — Aroma 5.12

Kwa Ine Imfa Idagonjetsedwa

Pakuti mphotho yake ya uchi-  
mo ndi imfa... — Aroma 6.23a

Potero usachite manyazi pa  
umboni wa Ambuye wathu, kape-

na pa ine wandende wake; koma-  
tu umve masautso ndi Uthenga  
Wabwino, monga mwa mpham-  
vu ya Mulungu; amene adatipulu-  
mutsa ife, natiitana ife ndi mai-  
tanidwe oyera, si monga mwa  
ntchito zathu, komatu monga  
mwa chitsimikizo mtima cha Iye  
yekha, ndi chisomo, chopatsika  
kwa ife mwa Khristu Yesu zisada-  
yambe nthawi zoyamba, koma  
chaonetsedwa tsopano m'maone-  
kedwe a Mpulumutsi wathu Khri-  
stu Yesu, amenedi adatha imfa,  
naonetsera poyera moyo ndi cho-  
sabhunda mwa Uthenga Wabwi-  
no. — 2 Timoteo 1.8-10

## **18 MFUMU ADAPERKA CHIPULUMUTSO CHAULERE KWA ONSE AMENE ACHIFUNA NDI MTIMA WONSE**

**1 Akorinto 15.3b**

...kuti Khristu adafera zoipa zathu, monga mwa malembo.

**Machitidwe A Atumwi 20.28b**

...kuti muwete Eklesia wa Mulungu, umene anaugula ndi mwazi wa Iye yekha.

**Yohane 10.11**

Ine ndine Mbusa Wabwino; mbusa wabwino ataya moyo wake chifukwa cha nkhosa.

Ndipo adafera onse, kuti iwo akukhala ndi moyo asakhalenso ndi moyo kwa iwo okha, koma kwa Iye amene adawafera iwo, nauka. — 2 Akorinto 5.15

**Machitidwe A Atumwi 10.43**

Ameneyu aneneri onse amchitira umboni, kuti onse akumkhu-lupirira Iye adzalandira chikhulu-lukiro cha machimo awo, mwa dzina lake.

Ambuye sazengereza nalo lonjeezano, monga ena achiyesa chizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena awonongeke, koma kuti onse afike kukulapa. — 2 Petro 3.9

**Yeremiya 29.13**

Ndipo mudzandifuna Ine, ndi kundipeza, pamene mundifuna ndi mtima wanu wonse.

## UDANI PAKATI PA MULUNGU NDI TCHIMO 19

Masalmo 45.6, 7a

Mpando wachifumu wanu, Mulungu, ukhala nthawi zonse zomka muyaya: Ndodo yachifumu ya ufumu wanu ndiyo ndodo yolunjika. Mukonda chilungamo, ndipo mudana nacho choipa...

1 Akorinto 6.9a

Kapena simudziwa kuti osalungama sadzalandira ufumu wa Mulungu? . . .

Aroma 8.5-8, 9b

Pakuti iwo amene ali monga mwa thupi asalalira zinthu za thupi; koma iwo amene ali monga mwa mzimu, asalalira zi-

nthu za mzimu: pakuti chisamaliro cha thupi chiri imfa; koma chisamaliro cha mzimu chiri moyo ndi mtendere. Chifukwa chisamaliro cha thupi chidana ndi Mulungu; pakuti sichigonja ku chilamulo cha Mulungu. Koma ngati munthu alibe Mzimu wa Khristu, siali wake wa Khristu.

Yakobo 4.4

Akazi achigololo inu, kodi simudziwa kuti ubwenzi wa dziko lapansi uli udani ndi Mulungu? Potero, iye amene afuna kukhala bwenzi la dziko lapansi adziika mdani wa Mulungu.

## 20 MOMWE TINGALANDILIRIDWE NDI MFUMU

Wobisa machimo ake sadzaona mwayi; Koma wakuwabvomereza, nawasiya adzachitidwa chifundo. — Miyambo 28.13

Ndipo ife tazindikira, ndipo takhulupirira chikondicho Mulungu ali nacho pa ife. Mulungu ndiye chikondi, ndipo iye amene akhala m'chikondi akhala mwa Mulungu, ndipo Mulungu akhala mwa iye. — 1 Yohane 4.16

### Yohane 1.12a

Koma onse amene adamlandira Iye, kwa iwo adapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu. . .

Machitidwe A Atumwi 10.35

Koma m'mitundu yonse, wa-

kumuopa Iye ndi wakuchita chilungamo alandiridwa naye.

Pakuti ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi, mudzafa; koma ngati ndi mzimu mufetsa zochita zake za thupi, mudzakhalala ndi moyo. — Aroma 8.13

### 1 Akorinto 2.5

Kuti chikhulupiro chanu chisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu.

### Yohane 8.31

Chifukwa chake Yesu adanena kwa Ayuda aja adakhulupirira Iye, Ngati mukhala inu m'mawu anga, muli akuphunzira anga ndithu.

# CHIPULUMUTSO UBALE WAMOYO NDI CHIYANJANO NDI KHRISTU

21

**Yohane 10.26-28**

Koma inu simukhulupira, chifukwa simuli a mwa nkhosa zanga. Nkhosa zanga zimva mawu anga, ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine. Ndipo Ine ndizipatsa moyo wosatha; ndipo sizidzawonongeka ku nthawi yonse, ndipo palibe munthu adzazikwatula m'dzanja langa.

**2 Timoteo 1.12**

Chifukwa cha ichicho ndinamva zoŵaŵa izi; komatu sindichita manyazi; pakuti ndimdziŵa Iye amene ndamkhulupirira, ndi-

po ndikopeka mtima kuti ali wa mphamvu ya kudikira chosungitsa changacho kufikira tsiku lijalo.

**1 Petro 4.19**

Koteronso iwo akumva zoŵaŵa munga mwa chifuniro cha Mulungu aike moyo wawo ndi kuchita zokoma m'manja a Wolenga wokhulupirika.

**Aefeso 3.19**

Ndi kuzama nchiyani; ndi kuzindikira chikondi cha Khristu, chakuposa mazindikiridwe, kuti mukadzazidwe kufikira chidzalo chonse cha Mulungu.

## 22 WOBADWANSO, WAUFULU KUTUMIKIRA AMBUYE

Yohane 1.13

Amene sanabadwa ndi mwazi, kapena ndi chifuniro cha thupi, Kapena ndi chifuniro cha muntu, koma cha Mulungu.

Ndipo mudzazindikira choonadi, ndipo choonadi chidzakumasulani. — Yohane 8.32

Yohane 8.36

Chifukwa chake ngati Mwana adzakuyesani inu afulu, mudzakhala mfulu ndithu.

Aroma 6.18, 22

Ndipo pamene mudamasulidwa kuuchimo, mudakhala akapolo a chilungamo. . . . Koma tsopano, pamene mudamasulidwa kuuchi-

mo, ndi kukhala akapolo a Mulungu, muli nacho chobala chanu cha Kufikira chiyeretso, ndi chimariziro chake moyo wosatha.

Koma ndani iye wolilaka dziko lapansi, koma iye amene akhulupirira kuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu? — 1 Yohane 5.5

Agalatiya 5.1

Khristu adatisandutsa mfulu, kuti tikhale mfulu; chifukwa chake chirimikani, musakodwenso ndi gori la ukapolo.

Machitidwe A Atumwi 22:15

Ndipo udzamkhalira Iye mboni kwa anthu onse, za izo udazi-ona ndi kuzimva.



## WOBADWA KACHIWIRI! TSOPANO NDINE YANI? 23

Chibvumbulutso 1.5b, 6

. . . Kwa Iye amene atikonda ife, natimasula ku machimo athu ndi mwazi wake; natiyesa ife ufumu fikhale ansembe a Mulungu ndiye Atate wake; kwa Iye kukhale ulemerero ndi mphamvu kufikira nthawi za nthawi. Amen.

1 Akorinto 6.9-11

Kapena simudziwa kuti osalungama sadzalandira ufumu wa Mulungu? Musasocheretsedwe; adama, kapena opembedza mafano, kapena achigololo, kapena olobodoka ndi zoipa, kapena akudziipsa ndi amuna, kapena ambala, kapena osirira, kapena oledzera, kapena olalatira, kape-

na olanda, sadzaloŵa Ufumu wa Mulungu. Ndipo ena a inu munali otere; koma mudasambitsidwa, koma mudayeretsedwa, koma mudayesedwa olungama, m'dzina la Ambuye Yesu, ndi mwa Mzimu wa Mulungu wathu.

Iwe udzakhalanso korona wokongola m'dzanja la Yehova, korona wachifumu m'dzanja la Mulungu wako. — Yesaya 62.3

Malo Okwezeka

Yohane 17.21a

Kuti onse akakhale amodzi, monga Inu Atate mwa Ine, ndi Ine mwa Inu, kuti iwonso akakhala mwa Ife. . .

## 24 WOPANGIDWA KUKHALA M'CHIYANJANO NDI MULUNGU

Masalmo 145.18

Yehova ali pafupi ndi onse akuitanira kwa Iye, Onse akuitanira kwa Iye m'choonadi.

Koma popeza mulaŵana ndi Khristu zoŵaŵa zake, kondwera ni; kutinso pa bvumbulutso la ulemmero wake mukakondwere kwakukurukuru. — 1 Petro 4.13

2 Akorinto 6:16

Ndipo chiphatikizo chake nchanji ndi kachisi wa Mulungu ndi wa mafano? Pakuti ife ndife kachisi wa Mulungu wamoyo; monga Mulungu adati, Ndidzakhaliŵa mwa iwo, ndipo ndidza-

yendayenda mwa iwo, ndipo ndidzakhala Mulungu wawo, ndi iwo adzakhala anthu anga.

1 Yohane 1.3b

...ndipo chiyanjano chathu chirinso ndi Atate ndipo ndi Mwana wake Yesu Khristu.

Yesaya 43.2

Pamene udulitsa pamodzi ndiri pamodzi ndi iwe; ndi pooloka mitsinje sidzakukokolola; pakupyola pamoto sudzapsya; ngakhale laŵi silidzakutentha.

Ine mwa iwo, ndi Inu mwa Ine, kuti akhale angwiro mwa mmodzi... — Yohane 17.23a

## UBALE PAKATI PA KHRISTU NDI OKHULUPIRIRA OONA

25

**Yohane 14.20**

Tsiku lomwelo mudzazindikira kuti ndiri Ine mwa Atate wanga, ndi inu mwa Ine, ndi Ine mwa inu. Lamulo Lake Lotsirizira Nkhaŵa Yathu Yoyamba

**Chibvumbulutso 22.17a**

Ndipo Mzimu ndi mkwatibwi anena, Idzani. . .

Chifukwa chake mukani, phunzitsami anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zime ne ndidakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndipo onani, Ine ndiri

pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira chimariziro cha nthawi ya pansi pano. — Mateyu 28.19, 20  
Chilungamo Cha Oyera Mtima  
Ndicho Chilungamo Cha  
Khristu Wokhala Mkati

**Akolose 1.27**

Kwa iwo amene Mulungu adafuna kuwazindikiritsa ichi chime ne chiri chuma cha ulemerero wa chinsinsi pakati pa amitundu, ndiye Khristu mwa inu, chiyembekezo cha ulemerero.

Pakuti Khristu ali chimariziro cha lamulo kulinga kuchilungamo kwa amene ali yense akhulupira. — Aroma 10.4

## 26 CHIFUNDO CHOTERE, CHIKONDI CHOTERE, CHISOMO CHOTERE!

1 Petro 1.3

Wodalitsika Mulungu ndiye Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, Iye amene, monga mwa chifundo chake chachikuru, anatibalanso ku chiyembekezo cha moyo, mwa kuuka kwa akufa kwa Yesu Khristu.

Aefeso 2.4-7

Koma Mulungu, wolemera chifundo, chifukwa cha chikondi chake chachikuru chimene adatikonda nacho, tingakhale tinali akufa m'zolakwa zathu, adatipatsa moyo pamodzi ndi Khristu (muli opulumutsidwa ndi chisomo), ndipo adatiukitsa pamodzi,

natikhazikitsa pamodzi m'zaku-mwamba mwa Khristu Yesu; kuti akaonetsere m'nyengo zirinkudza chuma choposa cha chisomo chake, m'kukoma mtima kwa pa ife mwa Khristu Yesu.

Ahebri 4.16

Potero tilimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wachisomo, kuti tilandire chifundo ndi kupeza chisomo cha kutithandiza nthawi yakusowa.

Ndipo ayesedwa olungama kwaulere, ndi chisomo chake, mwa chiombolo cha mwa Khristu Yesu. — Aroma 3.24

Agalatiya 4.4, 5

Koma pokwaniridwa nthawi, Mulungu adatuma Mwana wake, wobadwa ndi mkazi, wobadwa wakumvera lamulo, kuti akawombole iwo akumvera lamulo, kuti ife tikalandire umwana.

Iye wakulakika adzalandira izi; ndipo ndidzakhala Mulungu wake, ndi iye adzakhala mwana wanga. — Chibvumbulutso 21.7

Agalatiya 4.6, 7

Ndipo popeza muli ana, Mulungu adatumiza Mzimu wa Mwana wake alowe m'mitima yathu, wopfuula Abba, Atate. Koterokuti sulinso kapolo, koma

mwana; koma ngati mwana, woloŵa nyumbanso mwa Mulungu.

Ndipo ngati ana, pomweponso oloŵa nyumba; inde oloŵa nyumba ake a Mulungu, ndi oloŵa anzake a Khristu; ngatitu ife timva zoŵawa pamodzi naye, kuti tikalandirensu ulemerero pamodzi ndi Iye. — Aroma 8.17

1 Yohane 3.1a

Taonani, chikondicho Atate watipatsa, kuti titchedwe ana a Mulungu; ndipo tiri ife otere...

Agalatiya 3.29

Koma ngati muli a Khristu, muli mbewu ya Abrahamu, nyumba monga mwa lonjezano.

## 28 MULUNGU ADATSIMIKIZIRA CHIFANIZIRO CHAKE PA ANA AKE

Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwachitira ubwino, ndiwo amene aitanidwa monga mwa kutsimikiza kwa mtima wake. — Aroma 8.28, 29

Tumikirani Monga Khristu

Luka 22.27b

. . . koma Ine ndiri pakati pa inu monga ngati wotumikira.

Yendani Mu Chikondi Cha Khristu

Yohane 15.9

Monga momwe Atate wandikonda Ine, Inenso ndakonda inu; khalani m'chikondi changa.

Khalani Okhululukira

Luka 23.34a

Ndipo Yesu adanena, Atate, muwakhululukire iwo, pakuti sadiwa chimene achita . . .

Khalani Oleza Mtima Ndi Ofatsa  
2 Akorinto 10.1a

Koma ine ndekha Paulo, ndidandaulira inu mwa kufatsa ndi ulere wa Khristu . . .

Falitsani Uthenga Ku Dziko

Lonse Lapansi

Yohane 20.21

Chifukwa chake Yesu anatinso kwa iwo, Mtendere ukhale ndi inu; monga Atate wandituma Ine, Inenso ndituma inu.

**Kuti muyende koyenera Mulungu, amene akuitanani inu mulowê ufumu wake wa Iye yekha, ndi ulemerero.-1 Atesalonika 2.12**

**2 Yohane 9a**

**Yense wakupitirira, wosakhala m'chiphunzitso cha Khristu, alibe Mulungu. . . .**

**Khristu Adzakhala Ndi Mkwati-bwi Amene Sadzayesedwa  
Kapena Kukopedwa**

**Yakoba 1.12**

**Wodala munthu wakupirira poyesedwa; pakuti pamene wabvomerezeka, adzalandira korona wa moyo, amene Ambuye adalondejzera iwo akumkonda Iye.**

**Luka 6.47, 48**

**Munthu ali yense wakudza kwa Ine, ndi Kumva mau anga, ndi kuwachita, ndidzakusonyezani amene afanana naye. Iye afanafana ndi munthu wakumanga nyumba, amene anakumba pansi ndithu, namanga maziko a nyumbayo pathanthwe; ndipo pamene panadza chigumula, mtsinje unagunda pa nyumbayo, ndipo sunakhoza kuigwedeza; chifukwa idamangika bwino.**

**Tito 2.13**

**Akulindira chiyembekezo chodala, ndi maonekedwe a ulemerero wa Mulungu wamkuru ndi Mpulumutsi wathu Yesu Kristu.**

Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu: chiri mphatso ya Mulungu; chosachokera kuntchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense. — Aefeso 2.8-10

### 1 Akorinto 2.5

Kuti chikhulupiriro chanu chisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu.

### Aefeso 3.20, 21

Ndipo kwa Iye amene angathe kuchita koposa posatu zonse zimene tizipempha, kapena tiziganiza, monga mwa mphamvu ya kuchita mwa ife, kwa Iye ukhale

ulemerero mu Mpingo ndi mwa Khristu Yesu, kufikira mibadwo yonse ya nthawi za nthawi.

Adzapangidwa Kukhala Angwiro  
Ndi Athunthu Mwa Iye

### Aefeso 4.13

Kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa chikhulupiriro, ndi wa chizindikiritso cha Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Khristu.

Pakuti mwa Iye chikhalira chidzalo cha Umulungu m'thupi, ndipo muli odzazidwa mwa Iye, ndiye mutu wa ukulu wonse ndi ulamuliro. — Akolose 2.9, 10



## NDINE CHIWALO CHA MKWATIBWI WA MFUMU 31

Ndi Chifukwa Chiyani Iye Amene Angelo Osaŵerengeka Amampembedza Angakhazikitse Chikondi Chake Pa Munthu Waku-gwa Ndi Woukira?

### Ahebri 1.6

Ndipo pamene atenganso wobadwa woyamba kuloŵa naye m'dziko, anena, Ndipo amgwadire Iye angelo onse a Mulungu.

... chomwecho ife, ndife ambiri, tiri thupi limodzi mwa Khristu, ndi ziŵalo zinzake, wina ndi wina. — Aroma 12.5

... inunso munayesedwa akufa ku chilamulo ndi thupi la Khristu; kuti mukakhale ake a wina,

ndiye amene adaukitsidwa kwa akufa, kuti ife tim'balire Mulungu zipatso. — Aroma 7.4b

Mkwatibwi Alandira Moyo Kuchokera Kwa Iye

### 1 Yohane 5.12

Iye wakukhala ndi Mwana alinao moyo; wosakhala ndi Mwana wa Mulungu alibe moyo.

Chikondi Chathunthu Pa Mkwatibwi

Iye amene sadatimana Mwana wake wa Iye yekha, koma adampereka chifukwa cha ife tonse, adzalekeranji kutipatsano ife zinthu zonse kwaulere pamodzi ndi Iye? — Aroma 8.32

## 32 KUGAWANA MPANDO WACHIFUMU! NDI YANI, INE?

**Chibvumbulutso 3.21**

Iye wakulakika, ndidzampatsa akhale pansi ndi Ine pa mpando wachifumu wanga, monga Inenso ndidalakika, ndipo ndidakhala pansi ndi Atate wanga pa mpando wachifumu wake.

Mzinda Wa Mfumu Ndi  
Mkwatibwi

Koma tsopano akhumba lina loposa, ndilo la m'Mwamba; mwa ichi Mulungu sachita manyazi nawo poitanidwa Mulungu wawo; pakuti adawakonzera mudzi. — Ahebri 11.16

**Chibvumbulutso 3.12a**

Iye wakulakika, ndidzamyesa iye mzati wa m'Kachisi wa Mulu-

ngu wanga, ndipo kuturuka sadzaturukamonso; ndipo ndidzalembe pa iye dzina la Mulungu wanga, ndi dzina la mzinda wa Mulungu wanga, la Yerusalemu watsopano, wotsika m'Mwamba, kuchokera kwa Mulungu wanga...

Ndipo ndidaona mzinda woyerawo, Yerusalemu watsopano, ulikutsika Kumwamba kwa Mulungu, wokonzeka ngati mkwatibwi wokometsedwera mwamu na wake. — Chibvumbulutso 21.2

Odala iwo amene atsuka mii-njiro yawo, kuti akakhale nawo ulamuliro pa mtengo wa moyo, ndi kuti akaloŵe m'mzinda pazipata. — Chibvumbulutso 22.14

**Luka 16.11**

**Chifukwa chake ngati simudakhala okhulupirika m'chuma cha chosalungama, adzakhulupirira inu ndani ndi chuma choona?**

**2 Akorinto 8.9**

**Pakuti mudziwa chisomo cha Ambuye wathu Yesu Khristu, kuti, chifukwa cha inu adakhala wosauka, angakhale anali wolemera, kuti inu ndi kusauka kwake mukakhale olemera.**

**Mverani, abale anga okonde-dwa; kodi Mulungu sadasankha osauka a dziko lapansi akhale olemera ndi chikhulupiriro, ndi olowa nyumba a ufumu umene**

**adaulonjeza kwa iwo akumkonda Iye? — Yakobo 2.5**

**Zoopsya Za Chuma Cha  
Dziko Lapansi**

**Lamulira iwo achuma m'nthawi yino ya pansi pano, kuti asadzikuze, kapena asayembekeze-re chuma chosadziwika kukhala kwake Koma Mulungu, amene atipatsa ife zonse kochurukira, kuti tikondwere nazo; kuti achite zabwino, nachuruke ndi ntchito zabwino, nakondwere kugawira ena, nayanjane; nadzikundikire okha maziko okoma ku nyengo ikudzayi, kuti akagwire moyo weniweniwo. — 1 Timoteo 6.17-19**

## 34 TANTHAUZO LA CHUMA CHENICHENI KWA INE

Amene adzasanduliza thupi la-  
thu lopepulidwa, lifanane nalo  
thupi lake la ulemerero, monga  
mwa machitidwe amene akhoza  
kudzigonjetsera nawo zinthu  
zonse. —Afilipi 3.21

Akolose 1.12, 13

Ndi kuyamika Atate, amene  
adatiyeneretsa ife kulandirana na-  
wo cholowa cha oyera mtima  
m'kuunika; amene adatilanditsa  
ife ku ulamuliro wa mdima, nati-  
sunthitsa kutilowetsa m'ufumu wa  
Mwana wa chikondi chake.

Machitidwe A Atumwi 20.32

Ndipo tsopano ndikuikizani  
kwa Mulungu, ndi kwa mawu a  
chisomo chake, chimene chiri ndi

mphamvu yakumangirira ndi ku-  
patsa inu cholowa mwa onse oye-  
retsedwa.

Pamene Khristu adzaoneka,  
ndiye moyo wathu, pamenepo inu-  
nso mudzaonekera pamodzi ndi  
Iye m'ulemerero. — Akolose 3.4

Kuti amitundu ali olowa nyu-  
mba pamodzi ndi ife, ndi ziwa-  
lo zinzathu za thupilo, ndi ola-  
ndira nafe pamodzi palonjezano  
mwa Khristu Yesu, mwa Uthe-  
nga Wabhino... Kwa ine wo-  
chepa ndi wochepetsa wa onse  
oyera mtima adandipatsa chiso-  
mo ichi ndilalikire kwa amitu-  
ndu chuma chosalondoleka cha  
Khristu. — Aefeso 3.6, 8

## **NDIRI WOKONDWA INE NDINE WANU, AMBUYE! 35**

### **Masalmo 40.16**

Asekerere nakondwerere mwa Inu onse akufuna Inu: Iwo akukonda chipulumutso chanu asaleke kunena, Abuke Yehova.

Sekerani mwa Yehova, ndimo kondwerani inu olungama mtima; Ndipo pfulani mokondwera nonsenu owongoka mtima. — Masalmo 32.11

Kondwerani mwa Ambuye nthawi zonse: ndibwerezanso kuteri, kondwerani. — Afilipi 4.4

### **2 Akorinto 4.17**

Pakuti chisautso chathu chopepuka cha kanthawi chitichitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa ulemerero.

Kondwera kwambiri, mwana wamkazi wa Ziyoni; pfula mwana wamkazi wa Yerusalemu; taona, Mfumu yako ikudza kwa iwe; ndiye wolungama, ndi mwini chipulumutso... — Zekariya 9.9a

### **Luka 10.20**

Koma musakondwera nako kuti mizimu idakugonjerani, koma kondwerani kuti maina anu alembedwa m'Mwamba.

### **Masalmo 5.11**

Koma akondwere onse amene athawira kwa Inu, Apfula mokondwera kosaleka, popeza muwafungatira; Nasekere mwa Inu iwo akukonda dzina lanu.

## KODI MUNGAKANE CHIFUNDO CHAKE KWAMUYAYA?

Ahebri 12.25

Penyani musakane wolankhulayo. Pakuti ngati iwowa sadapululumuka, pomkana Iye amene adawachenjeza padziko, koposatu sitidzapulumuka ife, odzipatulira kwa Iye wa Kumwamba.

Yesetsani kulowa pa khomo lopapatiza; chifukwa anthu ambiri, ndikuuzani, adzafunafuna kulowamo, koma sadzakhoza. Pamene atauka mwini nyumba natseka pakhomo, ndipo inu mudzayamba kuima pabwalo, ndi kugogoda pachitseko, ndi kunena, Ambuye titsegulireni ife; ndipo Iye adzayankha nadzati ndi inu,

Sindidziwa inu kumene muchokera. — Luka 13.24, 25

Chifundo Chokanidwa Chingatembenukire Ku Mkwiyu

2 Atesalonika 2.10-12

Ndi m'chinyengo chonse cha chosalungama kwa iwo akuwonongeka, popeza chikondi cha choonadi sadachilandira, kuti akapulumsidwe iwo. Ndipo chifukwa chake Mulungu atumiza kwa iwo machitidwe a kusocheretsa, kuti akhulupirire bodza; kuti aweruzidwe onse amene sadakhulupirira choonadi, komatu adakondwera ndi chosalungama.

## KODI NDINE YANI POPANDA MFUMU IYI? 37

Wodzala Ndi Uchimo,  
Wotsutsidwa

**Yohane 3.18**

Wokhulupirira Iye saŵeruzidwa; wosakhulupira waŵeruzidwa ngakhale tsopano, chifukwa sadakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu.

Pakuti tikachimwa ife eni ake titatha kulandira chidziŵitso cha choonadi, sititsalanso nsembe ya kwa machimo, koma kulindira kwina koopsa kwa chiŵeruziro. . . . — Ahebri 10.26, 27a

Woŵeruzidwa Ndi Mawu

Iye amene akaniza Ine, ndi kusalandira mawu anga, ali naye

womweruza iye; mawu amene ndalankhula, iwowa adzamweruza tsiku lomariza. —Yohane 12.48

Wokondedwa Ndi  
Kufunafunidwa

Umo chidaoneka chikondi cha Mulungu mwa ife, kuti Mulungu adamantuma Mwana wake wobadwa yekha, aloŵe m'dziko lapansi, kuti tikhale ndi moyo mwa Iye. — 1 Yohane 4.9

**Chibvumbulutso 22.17**

Ndipo Mzimu ndi mkwati-bwi anena, Idzani. Ndipo wakumva anene, Idzani. Ndipo wakumva ludzu adze; iye wofuna, atenge madzi a moyo kwaulere.

## 38 MUNTHU ALI WOPUSA NGATI APITA KU GEHENA

Ndi Chopusa Kuwononga Umu-  
yaya Mu Chizunzo Ndi Satana  
Mu Gehena Pamene Ukadakhala  
Mu Chikondwerero Chosaneneka  
Mwa Khristu Kugawana Naye  
Mpando Wachifumu M'Mwamba  
Nthaŵi Za Nthaŵi

### Masalmo 53.1a

Chitsiru chimati mumtima  
mwake, Kulibe Mulungu. . .

Monga nkhwali iumatira pa  
mazira amene sidaikira, momwe-  
mo iye amene asonkhanitsa chu-  
ma, koma mosalungama; paka-  
ti pa masiku ake chidzamsiya iye,  
ndipo pa chitsirizo adzakhala wo-  
pusa. — Yeremiya 17.11

Koma Ambuye adati kwa Iye,  
Tsopano inu Afarisi muyeretsa  
kunja kwake kwa chikho ndi  
mbale, koma m'kati mwanu  
mudzala zolanda ndi zoipa. Opu-  
sa inu, kodi Iye wopanga kunja  
kwake sadapanganso m'kati mwa-  
ke? — Luka 11.39, 40

### Mateyu 7.26, 27

Ndipo yense akamva mawu  
anga amenewa, ndi kusawachita,  
adzafanizidwa ndi munthu wopu-  
sa, yemwe adamanga nyumba  
yake pamchenga; ndipo inagwa  
mvula, nidzala mitsinje, ndipo zi-  
dawomba mphepo, zinagunda pa  
nyumbayo; ndipo inagwa; ndi ku-  
gwa kwake kunali kwakukuru.



## GEHENA NDI DZENJE LA MULUNGU KUMENE 39 IYE AMAPONYA ZINYALALA

Ahebri 6.8

Koma ikabala minga ndi mitungwi, itayika; nitsala pang'ono ikadatembereredwa; chitsiriziro chake ndicho kutenthedwa.

Chibvumbulutso 14.11

Ndipo utsi wa kuzunza kwawo ukwera ku nthawi za nthawi; ndipo sapuma usana ndi usiku iwo akulambira chirombocho ndi fano lake, ndi iye ali yense akalandira lemba la dzina lake.

Mwana wa munthu adzatuma angelo ake, ndipo iwo adzasonkhanitsa pamodzi, ndi kucotsa mu Ufumu wake zokhumudwitsa zonse, ndi anthu akuchita kusa-

yeruzika, ndipo adzawataya iwo m'ng'anjo yamoto; kumeneko kudzakhala kulira ndi kukukuta mano. — Mateyu 13.41, 42

Afilipi 3.18b, 19a

...ali adani a mtanda wa Khristu; chitsirizio chao ndicho kuwonongeka...

Mulungu Ali Ndi Chidwi Chofuna Kuchita Zozizwitsa Kutiletsa Ife Kupita Ku Gehena, Monga Kukomana Ndi Gehena M'malo Mwathu, Kugonjetsa Imfa Ya Muyaya, Kuukanso Kuchokera Kwa Akufa Kuti Mwa Iye Tingapezemo Chigonjetso Ndi Kukhala Moyo.

## 40 MFUMU YA MAFUMU ADZAMPONYA SATANA MU NDEDE MWA KUFUNA KWAKE

Chibvumbulutso 20.1-3

Ndipo ndidaona mngelo ada-tsika Kumwamba, nakhala nacho chifungulo cha phompho, ndi unyolo waukuru m'dzanja lake. Ndipo anagwira chinjoka, njoka yakaleyo, ndiye mdierekezi ndi Satana, nammanga iye zaka chikwi, namponya kuphompho, natsekapo, nasindikizapo chizindikilo pamwamba pake, kuti asanyengenso amitundu kufikira kudzatha zaka chikwi; patsogolo pake ayenera kumasulidwa iye kanthawi.

Chibvumbulutso 20.7, 10

Ndipo pamene zidzatha zaka

chikwi, adzamasulidwa satana m'ndende yake... Ndipo mdierekezi wakuwasokeretsa adaponyedwa m'nyanja ya moto ndi sulfure, kumeneko kulinso chirombocho ndi mneneri wonyengayo; ndipo adzazunzidwa usana ndi usiku ku nthawi za nthawi.

Chigonjetso Chathunthu Ndipo  
Chamuyaya Pa Satana

Popeza tsono ana ndiwo a mwazi ndi nyama, Iyenso momwemo adalawa nawo makhali-dwe omwewo kuti mwa imfa akamuwononge iye amene anali nayo mphamvu ya imfa, ndiye mdierekezi. — Ahebri 2.14

## MUDZAMTUMIKIRA NDANI NTHAWI ZONSE? 41

Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa ambuye awiri: pakuti pena adzamuda mmodziyo, ndi kukonda winayo; pena adzakangamira kwa mmodzi, nadzanyoza wina. Simungathe kukhala kapolo wa Mulungu ndi wa Chuma. — Mateyu 6.24

Kodi Muli Kumutsata Satana Ku Ndende, Kapena Mfumu Ya Mafumu Ku Mpando Wake Wachifumu Ndipo Wamuyaya?

**Machitidwe A Atumwi 26.18**

Kukawatsegulira maso awo, kuti atembenuke kuchokera kumtima, kulinga kukuunika, ndi kuchokera kuulamuliro wa satana kulinga kwa Mulungu, kuti ala-

ndire iwo chikhululukiro cha machimo, ndi cholowa mwa iwo akuyeretsedwa ndi chikhulupiriro cha mwa Ine.

Koma amantha, ndi osakhulupira, ndi onyansa, ndi ambanda, ndi achigololo, ndi ambanda, ndi achigololo, ndi olambira mafano, ndi onse a mabodza, cholandira chawo chidzakhala m'nyanja yotentha ndi moto ndi sulfure... — Chibvumbulutso 21.8

**Yohane 8.34b, 36**

... ndinena kwa inu kuti yense wakuchita tchimo ali kapolo wa tchimolo. Chikukwa chake ngati Mwana adzakuyesani inu afulu, mudzakhala mfulu ndithu.

## 42 MADZI A MOYO AYENDELERA PA MAPAZI ANGA

### Yohane 4.10

Yesu adayankha nati kwa iye, Ukadadziwâ mtulo wa Mulungu, ndi Iye amene alinkunena ndi iwe, Undipatse Ine ndimwe; ukadapempha Iye, ndipo akadakupatsa madzi amoyo.

### Yohane 7.37

Koma tsiku lomariza, lalikirulo la phwando, Yesu adaimirira napfuula, ndi kunena, Ngati pali munthu akumva ludzu, adze kwa Ine, namwe.

### Chibvumbulutso 7.17

Chifukwa Mwanawankhosa wakukhala pakati pa mpando wachifumu adzawaweta, nadzawatsogolera ku akasupe a madzi a

moyo, ndipo Mulungu adzawapukutira misozi yonse pamaso pawo.

### Chibvumbulutso 22.1-3

Ndipo adandionetsa mtsinje wa madzi a moyo, wonyezimira ngati krustalo, oturuka ku mpando wachifumu wa Mulungu ndi wa Mwanawankhosa. Pakati pa khwalala lake, ndi tsidya ili la mtsinje, ndi tsidya lake lija pansi mtengo wa moyo wakubala zipatso khumi ndi ziwiri, ndi kupatsa zipatso zake mwezi ndi mwezi; ndipo masamba a mtengo ndiwo akuchiritsa nawo amitundu. Ndipo sipadzakhalanso themberero liri lonse...

# INU MUKUCHIPHONYA? MUFUNEFUNENI 43 NDI MTIMA WANU WONSE!

Mateyu 6.33

Koma muthange mwafuna U-fumu wake ndi chilungamo chake, ndipo zonse zimenezo zidza-wonjezedwa kwa inu.

Deuteronomo 4.29

Koma mukafuna Yehova Mulungu wanu kumeneko, mudzampeza, ngati mumfunafuna ndi mtima wanu wonse ndi moyo wanu wonse.

Miyambo 8.17

Akundikonda ndiwakonda; Akundifunafuna adzandipeza.

Luka 11.9

Ndipo Ine ndinena ndi inu, Pemphani, ndipo adzakupatsani; fu-

nani, ndipo mudzapeza; gogodani ndipo adzakutsegulirani.

Mudzibzalire m'chilungamo mukolole monga mwa chifundo; limani masala anu, pakuti yafika nthawi ya kufuna Yehova, mpaka afika Iye, nabvumbitsira inu chilungamo. — Hoseya 10.12

Yesaya 55.6

Funani Yehova popezeka Iye, itanani Iye pamene ali pafupi.

Masalmo 86.12

Ndidzakuyamikani, Ambuye, Mulungu wanga, ndi mtima wanga wonse; Ndipo ndidzalemekeza dzina lanu nthawi zonse.

## PHWANDO LA UKWATI — MULUNGU ATENGA MKWATIBWI!

Chibvumbulutso  
21.9b-11a, 22-24a

... ndidzakuonetsa mkwatibwi, mkazi wa Mwanawankhosa. Ndipo adanditenga mu Mzimu kunka ku phiri lalikuru ndi lalitali, nandionetsa mzinda wopatulikawo, Yerusalemu, wotsika m'Mwamba kuchokera kwa Mulungu, ndipo unakhala nawo ulemerero wa Mulungu. . . Ndipo sindinaona Kachisi momwemo; pakuti Ambuye Mulungu Wamphamvuyonse, ndi Mwanawankhosa ndiwo Kachisi wake. Ndipo pamzinda sipafunika dzuwâ, kapena mwezi wakuuwâlira;

pakuti ulemerero wa Mulungu uunikira umenewu, ndipo nyali yake ndiye Mwanawankhosa. Ndipo amitundu adzayendayenda mwa kuunika kwake . . .

Chibvumbulutso 19.7-9a

Tikondwere, tisekerere, ndipo tipatse ulemerero kwa Iye; pakuti wadza ukwati wa Mwanawankhosa; ndipo mkazi wake wadzi-konzera. Ndipo adampatsa iye abvale bafuta wonyezimira woti mbu; pakuti bafuta ndiye zolungama za oyera mtima. Ndipo adanena ndi ine, Lemba, Odala iwo amene aitanidwa ku phwando la ukwati wa Mwanawankhosa.

## KODI MKWATIBWI WA MULUNGU NDI WA MTUNDU WANJI?

45

Wodzipereka Kwa Iye

. . . koma mudzipereke inu no-  
kha kwa Mulungu, monga amo-  
yo ataturuka mwa akufa. . .

— Aroma 6.13b

Wokonda Mkwati

Akhale nacho chisomo onse  
akukonda Ambuye wathu Yesu  
Khristu m'chosawonongeka.

— Aefeso 6.24

Wodzalzidwa Ndi Chikondi Cha  
Umulungu

Koma iye amene akasunga  
mawu ake, mwa iyeyu zedi chiko-  
ndi cha Mulungu chathedwa. . .

— 1 Yohane 2.5a

M'modzi Ndi Iye

Pakuti tiri ziŵalo za thupi la-  
ke. — Aefeso 5.30

Wopanda Maŵangamaŵanga

Momwemo, okonedwa, pope-  
za muyembekeza izi, chitani cha-  
ngu kuti mupezedwe ndi Iye mu-  
mtendere, opanda banga ndi opa-  
nda chirema. — 2 Petro 3.14

Adzakhala Ndi Chisomo

Chenicheni

1 Petro 1.13b

. . . nimuyembekeze konse ko-  
nse chisomo chirikutengedwa ku-  
dza nacho kwa inu m'bvumbulu-  
tso la Yesu Khristu.

## 46 MFUMU AMAONONGA OUKIRA DZIKO LAPANSI

Iwo adzachita nkondo pa Mwanawankhosa, ndipo Mwanawankhosa adzaŵalaka, chifukwa ali Mbuye wa ambuye, ndi Mfumu ya mafumun...

—Chibvumbulutso 17.14a

Ndipo mngelo wolimba adanyamula mwala, ngati mphero yaikuru, naiponya m'nyanja, nana, Chotero Babulo, mudzi waukuru, udzapasulidwa kolimba, ndipo sudzapezedwanso konse. —Chibvumbulutso 18.21

Ndipo pamenepo adzabvumbulutsidwa wosayeruzikayo, amene Ambuye Yesu adzanthara ndi mzimu wa pakamwa pake, nadza-

muwononga ndi maonekedwe a kudza kwake.—2 Atesalonika 2:8

Ndipo mliri umene Yehova adzakantha nawo mitundu yonse ya anthu imene idathira nkondo pa Yerusalemu ndi uwu: nyama yawo idzaonda akali chiriri pa mapazi awo, ndi maso awo adzapuwala m'pfunkha mwawo, ndi lilime lawo lidzanyala m'kamwa mwawo. —Zekariya 14.12

Pomwepo pali chimariziro, pamene adzapereka ufumu kwa Mulungu, ndiye Atate, atatha kuthera chiŵeruzo chonse; ndi ulamuliro wonse, ndi mphamvu yomwe. —1 Akorinto 15.24



## **ZAKA CHIKWI (1,000) MKWATI NDI MKWATIBWI 47 AKUCHITA UFUMU PA DZIKO LAPANSI**

**Mateyu 6.10**

Ufumu wanu udze. Kufuna kwanu kuchitidwe, monga Kmwamba chomwecho pansi pano.

**Chibvumbulutso 11.15**

... Ufumu wadziko lapansi wanyamba kukhala wa Ambuye wathu, ndi wa Khristu wake: ndipo adzachita ufumu kufikira nthawi za nthawi.

**Chibvumbulutso 5.9b, 10; 20.4b**

... Chifukwa mwaphedwa, ndipo mwagulira Mulungu ndi mwazi wanu anthu a mafuko onse, ndi manenedwe onse, ndi mitundu yonse, ndipo mudawayesa iwo ufumu ndi ansembe kwa Mu-

lungu wathu; ndipo achita ufumu padziko . . . ndipo ndidaona mizimu ya iwo amene adawadula khosi chifukwa cha umboni wa Yesu, ndi chifukwa cha mawu a Mulungu . . . ndipo adakhala ndi moyo, nachita ufumu pamodzi ndi Khristu zaka chikwi.

**Chibvumbulutso 20.6**

Wodala ndi woyera mtima ali iye amene achita nawo pa kuka koyamba; pa iwoŵa imfa yachiwiri iribe ulamuliro; komatu adzakhala ansembe a Mulungu ndi a Khristu, nadzachita ufumu pamodzi ndi Iye zaka chikwizo.

## 48 MOYO WA NTHAWI ZONSE NDI MKWATI

Mulungu Ndi Ine Tikupita Popanda Malekezero, O Chimwemwe!

**Ndipo sikudzakhalanso usiku; ndipo sasowa kuunika kwa nyali, ndi kuunika kwa dzuwa; chifukwa Ambuye Mulungu adzawaunikira; ndipo adzachita ufumu ku nthawi za nthawi.**

— Chibvumbulutso 22.5

... chihema cha Mulungu chiri mwa anthu; ndipo adzakhalitsa nawo, ndi iwo adzakhala anthu ake, ndi Mulungu yekha adzakhala nawo, Mulungu wawo; ndipo adzawapukutira misozi yonse kuchotsa pamaso pawo; ndipo sipadzakhalanso imfa; ndipo sipadza-

khalanso maliro, kapena kulira, kapena choŵawitsa; zoyambazo zapita. — Chibvumbulutso 21.3b, 4

...ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka; pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakuwatulidwa nawo pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse. — 1 Atesalonika 4.16c, 17

Yohane 17.24a

Atate, amene mwandipatsa Ine, ndifuna kuti, kumene ndiri Ine, iwonso akhale pamodzi ndi Ine; kuti ayang'anire ulemerero wanga, umene mwandipatsa Ine.

## KHRISTU AKUTI

“Iye wakulakika, ndidzampatsa akhale pansi ndi Ine pa mpando wacifumu wanga, monga Inenso ndinalakika, ndipo ndinakhala pansi ndi Atate wanga pa mpando wa cifumu wace.”

—Cibvumbulutso 3.21



**Mwa Khristu Ndapangidwa Chifukwa Cha Zazikuru!  
Wangwiro Akundiitana Ndipo Ndiyenera Kupita,  
MPAKA KU CHIGONJETSO.**

Published in numerous languages by World Missionary Press as God supplies funds in answer to prayer. If you would like more copies for careful distribution, write in English or go to **[www.wmpress.org](http://www.wmpress.org)**.

**World Missionary Press, Inc.**  
**P.O. Box 120**  
**New Paris, Indiana 46553-0120 USA**